ZAMBIA LAW
DEVELOPMENT COMMISSION

# KACITIDWE KOSAVUTA KA DONGOSOLO LA MASANKHO (LOKONZEDWA) LA LAMULO NAMBALA 12 LA 2026

*A CiNyanja Version of the Simplified Electoral Process (Amendment) Act No. 12 of 2026*



## ABOUT THE ZAMBIA LAW DEVELOPMENT COMMISSION

The Zambia Law Development Commission, referred to as 'the ZLDC' or the 'Commission', is a semi-autonomous statutory body established under the Zambia Law Development Commission Act, Chapter 32 of the Laws of Zambia. The primary mandate of the Commission is law reform.

The functions of the Commission are to:

- Recommend the revision and reform of the law in Zambia;
- recommend the codification of unwritten laws in Zambia;
- review and consider proposals for law reform referred to the Commission by the Minister or the members of the public;
- holds seminars and conferences on legal issues;
- translate any piece of legislation into local languages; and
- research and make recommendations on

1. the socio-political values of the Zambian people that should be incorporated into legislation;
2. the anomalies that should be eliminated from the statute book;
3. new and more effective methods of administration of the law and the dispensation of justice that should be adopted and legislated;
4. the removal of archaic pieces of legislation from the statute book;
5. new areas of the law that should be developed, which are responsive to the changing needs of the Zambian society.

- encourage international co-operation in the performance of its functions under this Act, and
- do all such things incidental or conducive to the attainment of the functions of the Commission.

## COMPOSITION OF THE COMMISSION

The ZLDC is headed by a 13-member Commission composed of part-time members appointed by the Minister of Justice. The following are the members of the Commission:

| | | |
|---|---|---|
| i. Madam Justice Ruth Chibbabbuka | - | Chairperson |
| ii. Dr Chipo Mushota Nkhata | - | Vice Chairperson |
| iii. Dr O'Brien Kaaba | - | Committee Chairperson |
| iv. Mr Emmanuel Sibongo | - | Committee Chairperson |
| v. Ms. Bubala Chibbonta | - | Member |
| vi. Mrs. Kawama Goma Simumba | - | Member |
| vii. Mr Munukayumbwa Munyima | - | Member |
| viii. Ms. Mwaka Chizinga | - | Member |
| ix. Dr Herrick Mpuku | - | Member |
| x. Dr. Dominic Kangongo | - | Member |
| xi. Dr Bibian Kalinde | - | Member |
| xii. Mrs Eva Jhala | - | Member |
| xiii. Mrs Yvonne Wilombe Nakacinda | - | Member |

The day-to-day running of the Commission is undertaken by its Secretariat, which is headed by a Director who is also the Commission Secretary. Mrs Hope M. Ndhlovu-Chanda currently serves as Director and Commission Secretary.

**CODZIKANIRA**

Cofalitsidwa ici cakonzedwa ndi bungwe la Zambia Law Development Commission cabe ndi colinga cakuti anthu onse aphunzire ndi kuzindikira. Cikupereka kalongosoledwe ka kacitidwe Kosavuta Ka Dongosolo La Masankho (Lokonzedwa) La Lamulo Nambala 12 La 2026 kuthandiza mamembala a anthu onse pomvetsetsa mfundo zacikonzero zodziwikitsidwa mu Lamulo.

Colinga ca cofalitsidwa ici ndi gwero la maphunziro cabe ndipo silikupanga zolembedwa zokhazikitsidwa ndi lamulo. Siciyenera kudaliridwa ngati kuti uphungu walamulo kapena colowa m'malo ca Konsitityushoni ya Zambia [Yokonzedwa] ya Lamulo Nambala 13 ya 2025, monga momwe inakonzedwera, idzakhala tero.

Anthu pofuna cimasuliro kapena uphungu akulimbikitsidwa kufufuza za malamulo olinganizidwa kapena kupeza anthu anchito za malangizo a lamulo.

**CINYANJA**

## KACITIDWE KOSAVUTA KA DONGOSOLO LA MASANKHO (LOKONZEDWA) LA LAMULO NAMBALA 12 LA 2026

## PART I – PRELIMINARY PROVISIONS -MBALI 1 - ZOFUNIKA ZOYAMBIRIRA

### 1. Short Title - Mutu Waufupi

**Legal Text**

*This Act may be cited as the Electoral Process (Amendment) Act, 2026, and shall be read as one with the Electoral Process Act, in this Act referred to as the principal Act.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo limeneli lidzachedwa Kacitidwe Kosavuta ka Dongosolo la Masankho [Lokonzedwa] (Electoral Process [Amendment] Act).
Liyenera kuwerengedwa pamodzi ndi Dongosolo la Masankho limene lilipo.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Lamuloli silisintha lamulo lonse la Electoral Process Act. M'malo mwake, ilo likuwonjezera kapena kusintha mbali zinazake.

### 2. Amendment of Section 2 - Cikonzero ca Cigawo 2

**Legal Text**

*Section 2 of the principal Act is amended by the—*

*(a) deletion of the definitions of "campaign period", "candidate", "Code" and "presiding officer" and the substitution therefor of the following:*

*"campaign period" means the period commencing after the close of nominations and ending on the day preceding an election, as the Commission determines, in accordance with section 28;*

*"candidate" has the meaning assigned to the word in the Constitution and includes a person on a party list for a seat under the proportional representation electoral system in the National Assembly or a council;*

*"Code" means the Electoral Code of Conduct set out in the First Schedule;*

*"presiding officer" means a person appointed as presiding officer by the Commission under section 37B; and*

*(b) insertion of the following new definitions in the appropriate places in alphabetical order:*

*“adoption certificate” means a certificate signed by the president and secretary-general of a political party, or in the absence of the secretary-general, the president and deputy secretary-general of a political party, as prescribed, specifying a candidate who is sponsored by that political party for an election to the office of President, Member of Parliament, mayor, council chairperson or councillor;*

*‘deputy secretary-general’ means an office-bearer designated as deputy secretary-general, or an equivalent office-bearer, of a political party in accordance with the Societies Act;*

*“nomination petition” means a nomination petition filed in accordance with section 95A;*

*“party list” means a list prepared by a political party for the purposes of the proportional representation electoral system and submitted to the Returning Officer or a district electoral officer by a political party in accordance with section 36C;*

*“person with disability” has the meaning assigned to the words in the Constitution;*

*“president” means an office-bearer designated as president of a political party in accordance with the Societies Act;*

*“secretary-general” means an office-bearer designated as secretary-general, or an equivalent office-bearer, of a political party in accordance with the Societies Act; and*

*“youth” has the meaning assigned to the word in the Constitution.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

- **Nyengo ya kampeni** itanthauza nthawi imene imayamba pambuyo pa kulembetsa ndipo imatsekedwa patsiku lothera masankho asanacitike, monga mmene Commission lanenera pansi pa cigawo 28.
- **Munthu woima pa masankho** atanthauza— munthu amene akuimirira pa masankho a Prezidenti, Mpando wa Paliyamenti, kapena pa masankho Khansala a pansi pa dongosolo la munthu amene wapambana wonse; kapena munthu amene waphatikizidwa pa mndandanda wa cipani candale pa masankho a paliyamenti kapena local government pansi pa dongosolo la kuimira kolinganizidwa.
- **Khodi [Code]** litanthauza kacitidwe ndi kayendetsedwe ka masankho m’nthawi yoyamba [Electoral Code of Conduct].

- **Ofisala Woimira Masankho** atanthauza munthu wosankhidwa ndi Commission pansi pa cigawo 37B kuti ayang'anire poponya mavoti pa malo ocitira masankho.
- **Setifiketi ya Kuvomerezedwa** litanthauza setifiketi losanidwa ndi prezidenti ndi mlembi wa cipani candale, pa cipepala colinganizidwa, cotsimikiza kuti cipani candale calipirira/cikucirikiza munthu woima pa masankho a Prezidenti, Membala wa Paliyamenti, Meya, Wakumpando wa Khonsolo, kapena Khansala.
- **Pempho la Kulembetsa** litanthauza pempho laperekedwa ndi kusungidwa kulingana ndi cigawo 95A.
- **Mndandanda wa Cipani** litanthauza mndandanda wokonzedwa ndi cipani candale kuti ugwiritsidwe nchito dongosolo la masankho a kuimira kolinganizidwa ndi kuperekedwa kwa Ofisala Wobweza Masankho kapena a district electoral officer molingana ndi cigawo 36C.
- **Munthu woperewera kucita zinthu zina [wolemala]** lili ndi tanthauzo limene laperekedwa mu Konstityusheni.
- **Prezidenti** litanthauza munthu wodziwika wa cipani candale pansi pa lamulo la Societies Act.
- **Mlembi [Kalembera]** atanthauza munthu wodziwika ngati mlembi kapena kalembera, kapena munthu wokhala ndi udindo wofanna nawo, mu cipani pansi pa Societies Act.
- **Mnyamata** lili ndi tanthauzo loperekedwa pa mawu mu Konstityusheni.

## 2. Amendment of Section 12 - Cikonzero ca Cigawo 12

### Legal Text

*Section 12(2) of the principal Act is amended by the insertion of the word "new" immediately after the words "registration of".*

### Mawu Alamulo Osavuta Kumva

Kaperekedwe kameneka kasinthidwa mwakuwonjeza liwu "tsopano" pambuyo pa mawu "kalembetsedwe ka."

### Kodi Cimeneci Citanthauzanji?

Kumbuyoku, lamulo limalola bungwe la Commission kuletsa kulembetsa nthawi iliyonse pomwe masankho anali pafupi kucitika pofuna kukonzekera za masankho ndi kucita masankho. Pasi pa lamulo latsopano, pamene tsiku loponyera mavoti lalengezedwa, kulembetsa kwa masankho mu cigawo cimeneco kudzaimitsidwa kufikira cisankho cobwereza camalizidwa. Cimeneci citanthauza kuti anthu a mu cigawo ici sakwanitsa kulembetsa kukhala anthu oponya voti la cibwereza pa nthawi imeneyo, ngakhale kuti aloledwa kuponya mavoti kapena sanalembetse.

### 4. Amendment of Section 13 - Cikonzero ca Cigawo 13

**Legal Text**

*Section 13 of the principal Act is amended by the insertion of the following new subsections immediately after subsection (2):*

*(3) The Commission may determine the period within which the Provisional Register of Voters may be inspected.*

*(4) A registered voter may inspect, electronically, the Provisional Register of Voters during the period determined by the Commission under subsection (3).*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Cigawo 13 casinthidwa mwakuwonjezera magawo ang'onoang'ono atsopano. Lamulo latsopano likunena kuti bungwe la Electoral Commission lingaganize za nyengo [nthawi] pomwe Cikalata Coyembekezera ca Oponya Voti (Provisional Register of Voters) cidzategulidwa kuti anthuwo acione. Kuwonjezera pamenepo, anthu omwe analembetsa kukaponya mavoti amaloledwa kupenya [kapena kuona] pa zolembedwa zomwe zili mu Provisional Register pa itnaneti [online] m'kati mwa nthawi yoikidwa ndi bungwe la Commission.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cigawo 13 casintidwa mwakuwonjeza zigawo zina zatsopano. Zigawo zimenezo zinena kuti bungwe la Electoral Commission lingaganize za nthawi pomwe cikalata ca Provisional Register of Voters cidzatsegulidwa kuti anthu aonemo zomwe zinalembedwamo. Kuwonjezera pamenepo, anthu omwe analembetsa kudzavota amaloledwa kuona paokha mu cipepala ca Provisional Register pa intaneti [online] pa nthawi imene Commission yaika kucita zimenezi.

### 5.Amendment of Section 17(1) - Cikonzero ca Cigawo 17(1)

**Legal Text**

*Section 17(1) of the principal Act is amended by the deletion of the word "ninety" and the substitution therefor of the word "fourteen".*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Tsopano lamulo likunena kuti ngati munthu amene dzina lake mu cikalata ca Provisional Register of Voters ndipo dzina lake lalembedwa mosayenera, iyeyo ayenera kudziwitsa bungwe la Electoral Commission m'kati mwa masiku khumi ndi anai [14] m'malo mwa masiku makumi asanu ndi anai [90].

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Kusintha kumeneku kukutanthauza kuti anthu oponya mavoti ali ndi nthawi yocepa kwambiri yocitira lipoti zolakwika pa “maina awo” pa cikalata ca Provisional Register of Voters ku Commission. M’malo mokhala masiku 90 [makumi asanu ndi anayi, anthu ovota tsopano ali cabe ndi masiku kjhumi ndi anai [10] kuti anene za madandaulo awo kapena kukonza zolakwika. Cifukwa ca cimeneci, anthu ovota ayenera kukayang’ana mwamsanga pambuyo poti cikalatako cafalitsidwa ndi nkupereka lipoti la zolakwika zilizonse. Colinga ca kusintha kumeneku ndi kulumizitsa kalembetsedwe ndi kutsimikiza kacitidwe kameneka kotero kuti bungwe la Electoral Commission lingamalize nchito ya cipepala ca *voters’ register* m’nthawi yoyenera masankho asanacitike.

## 6. Amendment of Section 27 - Cikonzero ca Cigawo 27

**Original Provision**

*Section 27(1) of the principal Act is amended by the deletion of the word “section 20” and the substitution therefor of the word “section 24”.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo likusintha umboni wacigawo kucokera pa Cigawo 20 kukafika ku Cigawo 24.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci ndi kukonza komwe kumacitika potsimikiza kuti mfundo za lamulo zili m’cigawo coyenera.

## 7. Amendement of Section 28 - Cikonzero ca Cigawo 28

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Nthawi zoikidwa za masankho ndi kusintha kocitidwa ziyenera kufalitsidwa mu Government Gazette ndi mu manyuzipepala kapena m’zipangizo zazithunzi zosankhidwa ndi Electoral Commission.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Lamulo limafuna kuti Commission likonzekere ndondomeko ya nthawi ya masankho lisanafike tsiku loponya masankho. Ndondomeko imeneyi likuphatikizapo zinthu zofunika ndi zocitika ngati tsiku lotsekera kulembetsa masankho, kuyang’ana mu buku la maina a anthu ovota, masiku a kulembetsa, masiku a kampeni, ndi tsiku la cisankho ndi maola oponya cisankho. Ndondomeko imeneyi imafalitsidwa mu Government Gazettee.

Lamulo limalolanso kuti Commission lisinthe ndondomeko kulikonse monga mmene kungakhalire kuti masankhowo akhale omasuka ndi oyenera kapena komwe tsiku loponya masankho lasinthidwa.

Kusintha kwatsopano kukufuna kuti bungwe la Commission lifalitse ndi kukonza ndondomeko mu Government Gazettee ndi mu manyuzipepala omwe amalitsidwa kwambiri m'dziko lonse kapena kupyolera mu zipangizo zazithunzi zosankhidwa ndi Commission.

Cimeneci citanthauza kuti uthenga wa masankho tsopano ukugawidwa pa mitundu yambiri yofalitsira, kukhala kosavuta kuti anthu onse apeze masiku ofunika kwambiri a masankho ndi zilengezo, pomwe nthawi ikadaliko.

## 8. Amendment of Section 30 - Cikonzero ca Cigawo 30

### Mawu Alamulo Osavuta Kumva

Kaperekedwe kameneka kasinthidwa pofuna kudziwitsa zofunikira zatsopano kwa anthu olipiridwa poimirira pa masankho a cipani candale. Anthu amenewa oimirira pa masankho tsopano ayenera kutumiza setifiketi ya kusintha kwa civomerezo cocokera ku cipani cawo candale kukhala zipepala za mbali yawo yolembetsera. Cifukwa ca ciwonjezero cimeneci, ndime zomwe zili mu lamulo limeneli zalinganizidwa ndi kuikidwa manambala.

Kusintha kumafunanso kuti bungwe la Electoral Commission lifalitse mfundo za anthu olembedwa mu Government Gazettee kudzaima pa masankho, mu nyuzipepala yofalitsidwa m'dziko kapena kupyolera mu zipangizo za zithunzi zosankhidwa ndi bungwe la Electoral Commission. Kuwonjezera pamenepa, cifukwa ca lamulo latsopano lomwe laikidwamo, manambala a malamulo omwe alipo asintha, pomwe malamulo akale [2] ndi [3] tsopan akhala [3] ndi [4].

### Kodi Cimeneci Citanthauzanji?

Kumbuyoku, muntu wofuna kuimirira pa masankho ngati Prezidenti kapena Vaisi Prezidenti amafunika kutumiza mapepala olembetsera masankho, ndalama za masankho kusiyapo kokha Vaisi Prezidenti, kudziwitsa anthu za katundu yemwe ali naye ndi ngongole zake, kusaina afidaviti yowonetsa kuti munthuyo anali woyeneretsedwa kuimirira pa masankho, ndi cicirikizo cocokera kwa anthu dzana limodzi (100) olembetsedwa kukaponya voti wocokera ku Dera lililonse. Kusintha uku kumafuna kuti munthu wolipiridwa ndi cipani candale kuimirira pa masankho kuti atumize setifiketi yake yomuyenereza, kukhala umboni wakuti cipani camusankhadi kuti ndi munthu wawo woimirira pa cisankho.

Lamuloli limafunanso kuti bungwe la Electoral Commission lifalitse maina ndi mfundo za anthu olembetsedwa ndipo lifalitse zimenezi mu Gazette, manyuzipepala, kapena mu zipangizo za zithunzi. Kusintha kumeneku kumacititsa kuti dongosolo lamasnkho likhale loyera kwambiri ndipo

lolongosoka cifukwa setifiketi yoyenereza imathandiza kucinjiriza mikangano m'kati mwa zipani zandale pa anthu olembetsedwa, pomwe kufalitsidwa kwa uthengawu kumakweza kuona mtima ndi cidaliro ca anthu onse pa kacitidwe ka masankho.

## 9. Amendment of Section 31- Cikonzero ca Cigawo 31

### Mawu Alamulo Osavuta Kumva

Lamulo ili lasintidwa mwakuwonjezerako kamvedwe katsopano konena kuti pepala lolembetsera masankho ndi afidaviti ziyenera kutumizidwa pamodzi ndi setifiketi yoyenereza kwa munthu yemwe walipiridwa ndi zipani zandale, ngakhale kuti olembetsa masankho odziimira safunikira kupereka ciliconse. Kusintha uku kumafunanso kuti bungwe la Electoral Commission lifalitse mfundo za anthu onse olembetsedwa movomerezeka kumadera olembetsera.

### Kodi Cimeneci Citanthauzanji?

Kumbuyoku, lamulo ili limangofuna munthu kulembetsa kukaimirira pa masankho kupitira mu cipani candale kuti atumizenso setifiketi yacivomerezo kukhala umboni kuti cipani camusankha ndi kumusainira kuti aimirire m'malo mwa cipani cawo, pomwe anthu odziimira safunikira kukhala ndi setifiketi yacivomerezo cifukwa iwosakuimira cipani candale ciliconse ndipo akuimirira paokha, ndipo lamulo ili limafunanso kuti bungwe la Electoral Commission kulengeza kwa anthu onse zamfundo zonse zololedwa ndi anthu olembetsawo kumadera awo pofuna kukweza kuona mtima ndi kulola anthu onse kudziwa yemwe wavomerezedwa kuimirira pa masankho.

Cikonzero cimeneci cikupanga dongosolo lolembetsa kukhala lowona ndi lopereka cifukwa cake ndi kutsimikiza kuti anthu a cipani candale ndi ovomerezedwa ndi zipani zawo asanatengemo mbali m'masankho, kuthandiza kucepetsa msokonezo ndi mikangano pa munthu weniweni ali woimirira pa cipani, pomweponso kulola anthu onse kuona mosavuta maina ndi mfundo za omwe akwanitsa bwino kulembetsa.

## 10. Replacement of Section 33 - Mlowammalo, Cigawo 33

### Legal Text

*The principal Act is amended by the repeal of section 33 and the substitution therefor of the following:*

*33. (1) Subject to subsection (2), a candidate for election in a district or ward of a council shall lodge with the returning officer for that district or ward of a council that candidate's nomination paper and an affidavit in the prescribed manner and form.*

*(2) A nomination paper and an affidavit referred to under subsection (1) shall be accompanied by an adoption certificate, except that this requirement shall not apply to an independent candidate.*

*(3) The nomination paper referred to under subsection (1) shall be subscribed, in the presence of the returning officer for that district by at least fifteen persons registered as voters in the district in which a candidate is contesting an election.*

*(4) The nomination paper referred to under subsection (1) shall be subscribed, in the presence of the returning officer for that ward of a council, by at least nine persons registered as voters in the ward in which a candidate is contesting an election.*

*(5) A person appearing before a returning officer for the purpose of subscribing a nomination paper in accordance with subsection (3) or (4) shall produce a voter's card and a national registration card to the returning officer for inspection as proof of identity.*

*(6) A person qualifies to be a mayor or council chairperson if, in addition to the requirements set out under Article 154(2) of the Constitution, that person has a certificate of clearance showing the payment of council taxes, where applicable.*

*(7) The Commission shall publish the particulars of validly nominated candidates at the nomination centres.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo ili likulowa m'malo mwa Cigawo 33 ndipo limanena kuti munthu yemwe akuimirira ngati khansala, meya, kapena wakumpando ayenera kutumiza pepala lolembetsera ndi afidaviti kwa ofisala wobweza masankho mofunikira. Ngati munthuyo ndi wolipiridwa ndi cipani candale, kulembetsako kuyenera kuphatikizapo setifiketi yacivomerezo kucokera ku cipani cimeneco, koma anthu odziimira safunikira setifiketi imeneyi.

Pa masankho a cigawo [disitrikiti], pepala lolembetsera liyenera kucirikizidwa ndi anthu osacepera pa khumi ndi asanu [15] omwe ndi oponya voti olembetsedwa ocokera ku "wadi" limenelo. Pa masankho a cigawo [wadi], pepala lolembetsera liyenera kucirikizidwa ndi anthu osacepera pa khumi ndi asanu [9] omwe ndi oponya voti olembetsedwa ocokera ku "wadi" limenelo. Anthu ocirikiza ayenera kuonetsa khadi lolembetsera kuponya voti ndi NRC, kukhala umboni wotsimikizika.

Lamulo ili likunenanso kuti munthu yemwe akuimirira ngati meya kapena wakumpando wa khansala ayenera kukhala ndi setifiketi ya msonkho ya "council tax clearance certificate" ngati kungafunike. Kuwonjezera pamenepo, bungwe la Electoral Commission liyenera kufalitsa mfundo zonse za anthu amene ayeneretsedwa kuimirira, ku malo awo olembetsera.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Pansi pa lamulo lakale, mapepala olembetsera a masankho ku "wadi" amangofunika cicirikizo ca munthu olingalira, ndi womuthandiza, pamodzinso anthu olembetsedwa kukaponya mavoti ocokera ku wadi imeneyo. Lamulo latsopano lawonjezera nambala ya anthu ocirikiza [masapotazi] ofunikira. Pa masankho a cigawo [disitrikiti], pepala lombetsera tsopano nalonso liyenera kukhala locirikizidwa, pamaso pa ofisala wobweza masankho, ndi anthu osacepera pa anthu khumi ndi asanu [15] olembetsedwa wocokera kucigawo, pomwe pa masankho a wadi, ayenera kucirikizidwa ndi anthu osacepera pa anthu asanu ndi anai [9] olembetsedwa ocokera ku wadi. Anthu ocirikiza ayeneranso kuonetsa khadi lovotera ndi khadi la NRC, kukhala umboni wacizindikiro. Anthu olipiridwa ndizipani zandale ayeneranso kutumiza setifiketi ya civomerezo kucokera ku cipani cawo, pomwe anthu odzimiira safunikira kukhal ndi setifiketi imeneyi cifukwa ndi osalipiridwa ndi cipani candale.

Lamulo lakalele limafuna kuti munthu woimirira pa masankho ngati meya kapena wakumpando wa khonsolo akhale ndi setifiketi ya msonkho wakhonsolo wa tax clearence certificate ngati kungafunike, ndipo cimeneci capitiriza kukhala tere pansi pa lamulo latsopano. Komabe, lamulo latsopano limeneli lawonjezapo cinthu cina cofunikira ca Electoral Commission kuti lifalitse mfundo za anthu onse omwe analembetsa bwino m'malo awo olembetsera.

Cimeneci citanthauza kuti tsopano dongosolo lolembetsa likuphatikizapo kufufuza ndi kukhala ndi mpata ku uthenga wa anthu onse, comwe cingathandize kukonza kuona mtima ndi kutsimikiza zizindikiro ndi kuyenera kwa anthu oimirira pamodzi ndi owacirikiza awo.

**11. Insertion of Part IVA- Ciwonjezo ca Mbali IVA**

**Legal Text**

*The principal Act is amended by the insertion of the following new Part VIA immediately after Part IV called Proportional Representation system.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Mbali yatsopano, VIA, yawonjezedwa, imene ikudziwitsa dongosolo la Kuimiridwa Kolinganizidwa [Proportional Representation]. Pansi pa dongosolo la lamulo la kuimiridwa kolinganizidwa, Mipando yosungidwira azimayi, anyamata ndi anthu operewera pocita zinthu zina, adzatumizidwa ndi Electoral Commission pambuyo pa masankho m'kati mwa zipani. Cipani ciliconse cidzatenga mipando ingapo pakati pa mipando imeneyi, kulingana ndi kuculuka kwa mavoti omwe iwo analandira pa cisankho.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci citanthauza kuti lamulo lakale lasinthidwa mwakuwonjezera Mbali yatsopano VIA, pambuyo pa Mbali IV. Mbali imeneyi yatsopano ili ndi malamulo aang'ono okhudzana ndi dongosolo la Kuimiridwa Kolinganiza, limene ndi dongosolo la electoral commission mmene muli mipandoya zipani yoperekedwa ku zipani zandale kulingana ndi kuculuka kwa mavoti omwe iwo adzalandira pa masankho.

Konstityusheni ladziwitsa dongosolo la nambala yophatikizidwa pa masankho. Cimeneci citanthauza kuti mipando ina mu Paliyamenti ndi makhonsolo adzapitiriza kudzadzidwa kupyolera mu dongosolo la munthu wopambana onse pa masankho, pomwe, pomwe mipando yowonjezera azimayi, anyamata ndi anthu operewera kucita bwino zinthu zina.

Pansi pa dongosolo la wopambana ndi wopeza masankho masankho oculuka koposa anthu ena omwe anaimrira naye mu konsitichuwensi kapena mu "wadi". Dongosolo ili likadali cimodzimodzi pa masankho a mu makonsitichuwensi a Mamembala a Paliyamenti, meya, makhansala akumpando, ndi makhansala okhala m'mawadi.

Dongosolo latsopano la kuimira kolinganiza ndi losiyana cifukwa anthu sadzaponya mavoti awo mwacindunji a aliyense payekha kuti adzdze mipando yotsalira. M'malo mwake, zipani zandale zidzatumiza mndandanda wokhala ndi maina a azimayi, anyamata ndi anthu operewera kucita zinthu zina. Pambuyo pa masankho, bungwe la Electoral Commission lidzagawa mipando yosungidwa pakati pa zipani zandale kulingana ndi nambala ya mavoti.

**PART IVA PROPORTIONAL REPRESENTATION ELECTORAL SYSTEM**

**12. Section 36A – Eligibility for participation in proportional representation electoral system -**

**Legal Text**

*A political party that intends to contest for a seat under the proportional representation electoral system specified under Article 47(2)(b) and (3)(c) of the Constitution and in accordance with this Part shall have a candidate contesting for election as President.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo ili tsopano likunena kuti cipani candale comwe cifuna kudzaima pa masankho a dongosolo la kuima kolinganiza ayaneranso kukhala ndi munthu wodszaimirira ngati prezidenti.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Lemenli ndi lamulo lastopano lomwe linadziwitsidwa ndi kukonzans. Ilo limafuna cipani candale cimene cikufuna kuima pa masankho a mipando pansi

pa dongosola limasankho a kuimira kolinganiza kutinso akhale ndi munthu yemwe adzaimirira pa cisankho ca prezidenti. Cimeneci citanthauza kuti zipani zandale zakha zomwe zikutengamo mbali mu cisankho ca prezidenti zidzayeneretsedwa kulandira mipando pansi pa dongosolo loima molinganzidwa.

### 13.Section 36B – Formula and distribution of seats under proportional representation electoral system

**Legal Text**

*(1) The formula to be used by the Commission in the distribution of seats under the proportional representation electoral system is specified in the Second Schedule.*

*(2) The Commission shall, within seven days of the swearing in of the President-elect, distribute the seats under the proportional representation electoral system in the National Assembly and council, in proportion to the total number of valid votes received by a presidential candidate in the initial ballot.*

*(3) The Commission shall, where a political party refuses to take up a seat that has been distributed to that political party, re-distribute the vacant seat to a political party that qualified for a seat in line with the formula for distribution of seats referred to under subsection (1).*

*(4) The votes obtained by a presidential candidate of a political party that refuses to take up a seat under subsection (3), shall not be considered in the distribution of seats in accordance with this section.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo limeneli likunena kuti bungwe la Electoral Commission liyenera kugwiritsa nchito kacitidwe komwe kalimo mu mndandanda wa laumo la second schedule kugawa mipando ya kuimira kolinganiza M'nyumba Yamalamulo ndi makhonsolo pakati pa zipani kulingana ndi nambala yonse ya prezidenti pa mavoti olandiridwa pa nthawi yoyamba ya kuvota.

Bungwe la Commission liyenera kutsiriza kacitidwe kameneka m'kati mwa masiku asanu ndi awiri (7) pambuyo pasankhidwa kwa munthu wodzakhala Prezidenti kuti aluburitsidwe kukhala mu ofesi. Ngati cipani candale cakana kuwomereza mpando womwe capatsidwa, bungwe la Electoral Commission liyenera kupatsa (kupereka) mpando umenewo ku cipani cina comwe cinayerezedwa pogwiritsa nchito kacitidwe aka, m'njira yakuti cipani candale

cakana kutenga mpando, mavoti olandiridwa ndi munthu woima ngati presidenti wa cipanicimeneco, sadzawerengedwa pogawana mipando yotsalira.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Ili, ililonse lamulo latsopano lomwe lithanthauza kuti pambuyooa cisankho, bungwe la Electoral Commission Liyenera mwamsanga (m'kati mwa masiku asanu ndi awiri (7) kulumbiritsa Prezidenti) kugawa mipando ya kuimira kolinganizidwa mu Palyamenti ndi makhonsolo pogwiritisa nchito kacitidwe kolingana ndi kuculuka kwa mavoti omwe Prezidenti wacipani candale analandira m'masankho oyambirira. Zipani zomwe zili ndi mavoti oculuka cipezanso mipando yambiri ya kuimira kolinganiza.

Ngati cipani capatsidwa mpando koma cipanico cakana kutenga mpando, ndiye kuti mpandowo udzaoerekedwa ku cipatsidwa mpando koma cipanico cakana kutenga mpando, ndiye kuti mpandowo udzaperekedwa ku vipani cina comwe cayenerezedwa pansi pa malamulo amodzimodziwo, ndipo ngati cipani mpando, mavoti olandiridwa ndi munthu woimira pa Prezidenti wa cipani cimenecp sakhalanso akugwrirtsidwa nchtio pomwe akugawiranso mipando yotsalira. M'mawu osavuta kumva, lamulo ili likutsimikiza kuti mipando ikugawidwa motsatira mavoti, kudzadziwa mwamsanga, ndipo osawonongedwa ngati cipani cakana kutenga ,avoti amenewo.

**14. Section 36C – Submission of party list**

**Legal Text**

*(1) A political party shall, within seven days after the distribution of the seats in accordance with section 36B, submit a party list to the Commission in a prescribed manner and form on payment of a prescribed fee.*

*(2) A party list submitted under subsection (1) shall be signed by the president or secretary-general of a political party.*

*(3) A party list shall be submitted, in the case of a seat in —*

*(a) the National Assembly, to the Returning Officer; and (b) a council, to a district electoral officer.*

*(4) A political party shall not include, on a party list, a candidate who contested a seat under the first-past-the-post electoral system.*

*(5) A party list submitted under subsection (1) shall be accompanied by a consent form for each candidate, as prescribed, signed by the candidate appearing on the party list.*

*(6) The Commission shall, where a candidate on a party list submitted to the Commission dies, resigns from the political party that sponsored the candidate or is expelled from the political party before the publication of the names of Members of Parliament and councillors under the proportional representation electoral system, request the political party to submit an additional party list within a period determined by the Commission.*

*(7) The Commission shall publish the party list in accordance with section 36G as follows:*
*(a) in the case of a Member of Parliament, where a candidate on a party list submitted under subsection (1) meets the requirements specified under Article 70 of the Constitution; and*

*(b) in the case of a councillor, where a candidate on a party list submitted under subsection (1) meets the requirements specified under Article 153(4) of the Constitution.*

*(8) The Commission shall notify the political party to take remedial measures to rectify the party list within a period that the Commission may determine where —*
*(a) in the case of a Member of Parliament, a candidate on a party list submitted under subsection (1) does not meet the requirements specified under Article 70 of the Constitution; and*

*(b) in the case of a councillor, where a candidate on a party list submitted under subsection (1) does not meet the requirements specified under Article 153(4) of the Constitution.*

*(9) The Commission shall, where a political party does not submit a party list within a period specified under this section, re-distribute the vacant seat to a political party that qualified for a seat in line with the formula for distribution of seats under section 36B.*

*(10) The votes obtained by a presidential candidate of a political party that does not submit a party list under subsection (9), shall not be considered in the distribution of seats.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo ili ndi latsopano ndipo limena kuti cipani candale ciyenra kupereka mndandanda wake wocipani ku bungwe la Elecotoral Commission m'kati mwamasiku asanu ndi awiri (7) pambuyo pakuti mipando yagawidwa. Mndandanda umenewu uyenera kukhala pa fomu, ndipo cipani ciyenera kulipira ndalama.

Mndandanda wa cipani uyunera kusaiwidwa ndi Prezidenti kapena mlembi (kalmembera). Cimeneci cionetsa kuti mndandanda umwenewo ndi "woyeneradi" ndipo wavomerezedwa atsagoleri acipani.

Pa mipando ya Paliyamenti, mndandanda wacipani uyenera kupatsidwa kwa ofisala wobweza Masankho (Returning Officer). Pa mipando ya khonsolo, mndadanda uyenera kupatsidwa kwa District Electoral Officer.

Cipano candale sicingaphatikize munthu wina amene watengamo kale mbali m'masankho pansi pa dongosolo la woyamba wopambana ena onse. Cimeneci citanthauza kuti munthu m'modzi sangatengemo mbali m'mitundu yonse ya madongosolo pa nthawi imodzi.

Munthu aliyense woima pa masankho yemwe ali pa mndandanda wa cipani ayeneranso kusaina cipepala cacilolezo. Cimeneci cithanthauza kuti munthu woima pa masanhko ayenra kumvomereza kusaina pa mndandanda umenewo.

Ngati munthu woima pa masankho wafa, watula udindo kucoka mu cipani, kapena watulutsidwa pomwe maina asafalitsidwe, bungwe la Commission lingapemphe cipani kuti citumize mndandanda wina kuladakali nthawi imene cipanico cayika.

Bungwe la Commission lidzafalitsa mndandanda wa cipani pokhapo ngati anthu oima pa masankho ali ndi zofunukura za lamulo la mpando wa Paliyamenti kapena khonsolo.

Ngati munthu woima pa masankho sakukwanitsa zofunikira bungwe la Commission Lidzauza cipani kuti cikonze mndandandandao m'kati mwa nthawi yoikidwa, ndipo ngatio cipawi cilephera kutumiza mndandanda wake pa nthawi yoyenera, mpando wopanda munthu udzapatsidwa ku cipani cina cimene cinayenerezedwa pansi pa kacitidwe ka kagawidwe ka mipando. Kuwonjezera pamenepa, ngati cipani cilephera kutumiza mndandanda wake, mavoti ake munthu woimiriria ngati prezidenti anapeza sadzawerengedwa psgawa mipando.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Ili ndi lamulo latsopano lodziwitsidwa ndi kukonzedwa kocirikiza dongosolo la masankho a kuimira kolinganizidwa. Lamulo lakale linalibe malamulo ang"ono onena za mndandanda wa cipani cifukwa kunalibe mipando ya kuimira kolinganizidwa.

**Mndandanda wacipani** utanthauza mndandanda wokonzedwa ndi cipani kuti ugwiritsidwe nchito pa dongosolo la kuimira kolinganizidwa ndipo umatumizidwa kwa Wobweza Masankho [Returning Officer].

Lamulo latsopano likupereka dongosolo ku zipani zandale kuti zilondole pomwe zikutumiza mndandanda wacipani pa mipando yosungidwa pansi pa dongosolo

la kuimira kolinganizidwa. Lamulo ili likulongosola amene ayenera kusaina pa mndandanda wacipani, komwe uyenera kutumizidwa, m'kati mwa nthawi imene unafunika kuikidwa mu faelo, ndipo zofunikra za anthu oima pa masankho zoyenera kucita. Likulongosolanso comwe cimacitika ngati mutu woima pa masankho wafa, wasiya cipani candale, kapena ngati kuti cipani calephera kutumiza mndandanda pa nthawi yoyenera.

Cimeneci citanthauza kuti tsopano lamulo likupereka dongosolo la mmene mipando kuimira kolinganizidwa idzacitidwira, kuperekedwera, ndi kudzadzidwira pomwe ikuthandiza kutsimikiza.

### 15. Section 36D – Requirements of party list for seat in National Assembly

**Legal Text**

*(1) A political party that submits a party list in accordance with section 36C for a seat in the National Assembly shall submit a party list for each category as follows:*

*(a) the number of women seats obtained by a political party;*

*(b) the number of youth seats obtained by a political party; and*

*(c) the number of persons with disabilities seats obtained by a political party.*

*(2) A party list submitted under subsection (1)(b)shall contain candidates that are youths for the entire duration of the term of Parliament.*

*(3) A party list submitted under subsection (1)(c) shall —*

*(a) contain alternates of the classes of disabilities; and*

*(b) have candidates in possession of a certificate of registration issued in accordance with the Persons with Disabilities Act.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo latsopan likunena kuti pamene cipani candale cilandira mipando M'nyumba Yamalamulo [Paliyamenti] kupitira mu dongosolo la kuimira kolinganiza, liyenera kutumiza mndandanda wacipani pa mbali iliyonse, ya azimayi, anyamata, ndi anthu operewera kucita zinthu zina. Mndandanda wa anyamata uyenera kuphatikizapo anthu oima pa masankho omwe ndi anyamata kwa utali wonse wa Paliyamenti. Mndandanda wa anthu operewera kucita zinthu zina uyenera kuphatikizapo anthu oima pa masankho m'magulu osiyanasiyana, ndipo anthu oima pa masankho pa mndandandawo ayenera kukhala ndi masetifiketi olembetsera a Regisration Certificates pansi pa Lamulo la Persons with Disabilities. Mindandanda iyi, pambuyo pake imatumizidwa ku bungwe la Electoral Commission, lomwe limagnizira kuti ndani amene ayenera kudazadza mipando yapadera mu Paliyamenti.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Kumbuyoku, lamulo linalibe kalongosoledwe kameneka. Lamulo latsopano litanthauza kuti zipani zandale sizingasankhe anthu kuti akhale pa mipando yapadera popanda kutsatira malamulo olinganizidwa. M'malo mwake, iwo ayenera kukonza mndandanda wacipani wa gulu lililonse, la azimayi, la anyamata, ndi la anthu operewera kucita zinthu zina. Bungwe la Electoral Commission pambuyo pake lidzagwiritsa nchito mindandanda imeneyi kudziwa kuti ndani ayenera kukhala m'mipando imeneyo.

Lamulo limeneli limafunanso anyamata pa mndandanda wa anyamatakuti ukhale m'kati mwa msinkhu woyenera kupitirira utali wonse wa nyengo ya paliyamenti. Kuwonjezera pamenepa, mndandanda wa anthu operewera pocita zinthu zina uyenera kulembetsedwa ndipo uyenera kuimira mitundu yosiyanasiyana ya kulephera kumeneku.

Cimeneci caikidwa kuti citsimikize kuti magulu omwe kawirikawiri sakuimiridwa mokwanira pautsogoleri, monga azimayi, anyamata ndi anthu operewera kucita zinthu zina, akuimiridwa mu Paliyamenti.

Cimeneci citanthauza kuti kacitidwe kodzadza mipando yosungidwa ndi kolongosoka ndi kokonzedwa bwino, kokhala ndi malamulo ang'ono ofuna kukweza ndi kukhala kulinganiza kophatikizidwa.

**16. Section 36E – Number of councillors under proportional representation electoral system -**

**Legal Text**

*(1) The number of councillors under the proportional representation electoral system in a council shall be calculated based on the eighteen percent of the proportional representation seats against constituency based seats in the National Assembly.*

*(2) The number of seats under the proportional representation electoral system in a council shall be distributed among women, youth and persons with disabilities using the ratio four to three to one, respectively, except that each category of women, youth and persons with disabilities shall have at least one seat.*

*(3) Despite subsections (1) and (2), a council shall, where the proportional representation seats in a council is less than three in accordance with the calculation referred to under subsection (1), consist of three proportional representation seats comprising of one seat for women, youth and persons with disabilities, respectively.*

*(4) The Commission shall publish the number of proportional representation seats in each council in accordance with this section, as prescribed*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo ili likulongosola mmene mipando yapadera ya khonsolo mu khonsolo amagawidwira pakati pa magulu osiyansiyana. Coyamba, nambala ya makhonsolo a kuimira kolinganizidwa imawerengeredwa pogwiritsa nchito fomyula yozikidwa pa 18% [peresenti] ya mipando ya mu konsitichuwensi mu National Assembly. Pamene nambala yonse ya mipando imeneyi yatsimikizidwa, iyo pambuyo pake imagawidwa pakati pa magulu atatu, okhala ndi azimayi], anyamata, ndi anthu operewera kucita zinthu zina, pa resho ya azimayi anayi [4], anyamata atatu [3], ndi munthu mmodzi wa anthu operewera kucita zinthu zina, akutsimikizira kuti gulu lililonse lidzapeza mosacepera pa mpando umodzi ngakhale kuti manambala awo ndi ocepa. Pa zocitika zimenezi, pomwe nambala yonse ya kuimira kolinganizidwa mu khonsolo ndi yocepera ndi zitatu [3], lamulo limafunabe kuti pakhale mipando yosacepera pamipando itatu [3], ndi mpando umodzi woperekedwa ku gulu lililonse. Bungwe la Electoral Commission lili ndi udindo wolengeza ndi kufalitsa nambala ya mipando ya kuimira kolinganizidwa ku khonsolo lililonse kulingana ndi lamulo.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci citanthauza kuti lamulo latsopano likulimbikitsa kuphatikiza kuimirdwa kwa makhonsolo mwakutsimikizira kuti azimayi, anyamata, ndi anthu operewera kucita zinthu zina onse pamodzi ndi oimiridwa, ngakhale pomwe mipando imene ilipo ndi yocepa, kotero kuti palibe gulu lililonse lomwe lasiidwa. Lamulo limeneli likumbikitsa ulamuliro wophatikizidwa mwakutsimikiza kuti magulu awa ali ndi liwu pa kacitidwe kopanga maganizo,

**17. Section 36F – Requirements of party list for seat in council**

**Legal Text**

*(1) Subject to section 36E, a political party that submits a party list in accordance with section 36C for a seat in a council shall submit a party list for each category as follows:*

*(a) the number of women seats obtained by a political party;*

*(b) the number of youth seats obtained by a political party; and*

*(c) the number of persons with disabilities seats obtained by a political party.*

*(2) A party list submitted under subsection (1), in relation to youths, shall have candidates that are youths for the entire duration of the term of a council.*

*(3) A party list submitted under subsection (1) in relation to persons with disabilities shall—*

*(a) contain alternates of the classes of disabilities; and*

*(b) have candidates in possession of a certificate of registration issued in accordance with the Persons with Disabilities Act.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo ili litanthauza kuti pomwe cipani candale cikupereka maina a mipando mu khonsolo, liyeneranso kutumiza mndandanda umodzi cabe. M'malo mwake, liyenera kukonzekera kupatula mindandanda ya cipani pa gulu lililonse lapadera la mipando yomwe yapambana, ngati mipando ya azimayi, mipando ya anyamata ndi mipando yaanthu operewera kucita zinthu zina. Mawu akuti, "motsatira cigawo 36E" atanthauza kuti lamulo ili liyenera kuwerengedwa pamodzi ndi cigawo 36 E, ndipo kuti cigawo cimeneco cikupereka lamulo lapadera kapena malire ("limitation"), omwe adzakhudza malamulo ena. M'mawu osavuta, cipani ciyenera kufananitsa nambala ya mipando yosungidwa yomwe yapeza mu gulu lililonse.

Kugulu la anyamata, lamulo likufuna zambiri zoposa kungoika munthu wacicepere pa mndandanda pa nthawi ya kulembetsa. Limanena kuti anthu omwe ali mu cipani ayenera kukhala anyamata pa utali wonse wa nyengo ya khonsolo. Cimeneci citanthauza kuti munthu yemwe wasankhidwa ayenera kupitiriza kukhala mnyamata kukafika kumapeto kwa utali wa nthawi ya khonsolo. Colinga cake ndi kutsimikiza kuti mpando umenewo ukupitiriza kugwiritsidwa nchito ndi winawake amene zoonadi ali pagulu la anyamata, osati munthu wina yemwe anayenerezedwa poyamba koma salinso pamenepo.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Lamulo ili likukweza kuimirira kophatikizidwa m'makhonsolo mwakutsimikiza kuti azimayi, anyamata ndi anthu operewera kucita zinthu zina amapatsidwa mipando yosungidwira boma laling'ono [local government]. Cotero, zipani zandale zifunikira kuphatikiza magulu awa mu pa utsogoleri ndi dongosolo lopanga maganizo, comwe cimathandiza kulinganiza ndi kutengamo mbali kwa magulu omwe kawirikawiri saimiridwa mokwanira. Zipani zandale ziyenera kulondola ndondomeko yolimba pokonza ndandanda zawo. Iwo ayenera kutumiza ndandanda zosiyana pagulu lililonse ndi kutsimikiza kuti oima pa masankho a khonsolo, pomwe anthu ena acinyamata adzakhala acinyamata panyengo yonse ya nthawi ya khansala, pomwe anthu operewera kucita zinthu zina ayenera kukhala masetifiketi olembetsera oyenera. Cimeneci cimawonjezera kuwerengera, kucepetsa dongosolo lowononga, ndi kutsimikiza kuti mipando yosungidwa idzagwiritsidwa nchito ndi anthu oyenerera.

Lamulo ili likulimbikitsa kuimira kolingana, makamaka pakti pa anthu operewera kucita zinthu zina, mwakufuna kuphatikiza mitundu yosiyanasiyana ya kuperewera kucita zinthu zina. Koma, cimeneci cidzacititsa kuti pakhale vuto la kuyang'anira ndi mavuto ku zipani zandale, makamaka zipani zazing'ono,

cifukwa izo ziyenera kusamala nkhope ya muntu, kutsimikiza ndi kusunga anthu oyenerera pa masankho pa magulu onse osungidwa.

### 18. Section 36G – Publication of party list

**Legal Text**

*The Commission shall, within seven days of the receipt of a party list in accordance with section 36C, process and publish the names of Members of Parliament and councillors that obtained a seat under the proportional representation electoral system in the Gazette, and a newspaper of general circulation in the Republic or any electronic media that the Commission may determine.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Bungwe la Commission liyenera kugwira nchito m'kati mwa masiku asanu ndi awiri [7] pambuyo polandira mndandanda wacipani pansi pa Cigawo 36 C. Limeneli ndi dongosolo lofunika pokonza mndandanda ndipo ndi kufalitsa maina a Mamembala a Paliyamenti ndi makhonsolo amene apatsidwa mipando kupyoleam'dongosolo la kuima kolinganiza. Maina ayenera kufalitsidwa kotero kuti anthu onse mu Government Gazette, mu nyuzipepala imene imawerengedwa ndi anthu ambiri m'dziko lonse, kapena kupyolera mu zipangizo za zithunzi zomwe bungwe la Commisson lasankha.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci citanthauza kuti bungwe la Electoral Commission lifuna kugwira nchito m'kati mwa nyengo ya masiku asanu ndi awiri [7] yolandira mndandanda wacipani. Lamulo ili likulimbikitsa kuona mtima, kuwerengera, ndi kugwira bwino nchito m'dongosolo la ponya masankho mwakutsimikiza kuti za nthawi yocitira nchito ndi kulengeza za mipando yoperekedwa. Limafunanso kufalitsidwa kwa maina a Mamembala a Paliyamenti ndi makhonsolo mu Government Gazette, manyuzipepala ofalitsidwa kwambiri, kapena cipangizo ciliconse ca zithunzi cosankhidwa ndi Commission, cotero kutsimikiza kuti zotsatira za cisankho zafika, mosavuta kwa aliyense.

### 19. Section 36H – Vacancy in office of Member of Parliament under proportional representation electoral system

**Legal Text**

*(1) Article 72(1) and (2)(a), (b), (c), (d), (e), (f), (h) and (i) of the Constitution shall apply in relation to a vacancy of a Member of Parliament under the proportional representation electoral system.*

*(2) In addition to the grounds specified under subsection (1), a political party that sponsored a Member of Parliament holding a seat under the proportional representation electoral system may recall the Member of Parliament at any time during the term of Parliament.*

*(3) A person who causes a vacancy in the National Assembly due to the reasons specified under Article 72(2)(a), (b), (c), (d) and (h) of the Constitution shall not, during the term of that Parliament —*

*(a) be eligible to contest an election or qualify to be on a list under the proportional representation electoral system; or*

*(b) hold public office.*

*(4) The Speaker shall, where a vacancy occurs in the National Assembly for a seat under the proportional representation electoral system, inform the Commission of the vacancy, in writing, within seven days of the occurrence of the vacancy.*

*(5) The Commission shall, within ninety days of the vacancy in accordance with subsection (1) or (3), fill the vacancy with the next available candidate on a party list of a political party that holds the seat.*

*(6) The Commission shall, where a party list of a political party has no remaining candidate during the term of Parliament, request the political party to submit an additional party list within thirty days of the request.*

*(7) Sections 36C and 36D shall apply to an additional party list referred to under subsection (6).*

*(8) The Commission shall, where a political party fails to submit an additional party list within the period specified under subsection (6), re-allocate the vacant seat to a political party that qualified for a seat in accordance with the formula for distribution under section 36B.*

*(9) The votes obtained by a presidential candidate of a political party that fails to submit an additional party list under subsection (8) shall not be considered in the distribution of seats.*

*(10) A Member of Parliament holding a seat for a political party under the proportional representation electoral system shall, where a political party is dissolved, cease to be a Member of Parliament and the seat shall be re-allocated to a political party that qualifies for a seat in line with the formula for distribution of seats under section 36B.*

*(11) A vacancy occurring in accordance with this section within one hundred and eighty days preceding a general election shall not be filled.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo ili linena za zomwe zimacitika pomwe mpando mu paliyamenti wosungidwa kupitira mu dongosolo la kuimira kolinganiza, wakhala wopanda munthu, ndipo mmene mpandowo ungalowedwere m'malo. M'mawu osavuta, ilo limanena kuti Mamembala a Paliyamenti osankhidwa kupyolera pa Kuimira Kolinganizidwa amakhalabe pansi pa konsitityushoni ngati wina walephera kupambana pa mpando, koma palinso malamulo apadera a mndandanda wa zipani, mwambo wa cipani, kulowedwa m'malo, ndi malo opanda mwini ocedwa.

Coyambirira, mbali ya cigawo (1) imatanthauza kuti zifukwa za nthawi zonse za konsitityushoni kuti mpando wa MP ukhale wopanda munthu pansi pa kuimira kolinganiza. Zifukwa zimenezo zimaphatikizapo kutula udindo, kusayenerezedwa, khalidwe loipa, kusiya kapena kucotsedwa mu cipani comulipirira munthu, kuleka kukhala nzika, kusayenerezedwa ndi bwalo la Konsitityushono khoti, ndi imfa. Zotsatira zake ndi zakuti Membala wa Paliyamenti osankhidwa kupitira mu Kuimira Kolinganizidwa samacitiridwa ngati kuti iye ndi wacikhalire cifukwa cakuti iye analowa mu Paliyamenti kupitira mu mndandanda wacipani.

Caciwiri, mbali ya cigawo (2) imawonjezera lamulo lina lomwe ndi lacindunji pa kuimira kolinganiza: cipani candale comwe cinalipirira MP cingaitane MP ameneyo pa nthawi iliyonse pomwe Paliyamenti ikugwira nchito. M'mawu osavuta, cipani cingacotse Mamembala ake a Paliyamenti osankhidwa kupitira mu Kuimira Kolinganizidwa ngakhale kuti palibe zifukwa zenizeni za lamulo zomwe zacitika. Cimeneci cikupatsa cipani mphamvu zazikulu pa anthu ake osankhidwa m'mipando kupitira mu Kuimira Kolinganizidwa mosiyana ndi masankho a mipando ya konsitityuwensi.

Cacitatu, mbali ya Cigawo (3) imanena kuti ngati munthi wacititsa kuti pakhale mpandp wopanda mwini cifukwa ca zifukwa zolembedwa munthu ameneyo ayenera kulangidwa pa nthawi yomwe Paliyamenti ikuletsedwa kupikisana pa cisankho kapena kukhala pa m'ndanda wa kuimira kolinganiza, ndipo kumwetsa kuti asakhale ndi ofesi yaikulu. Conco lamulo pano Likuyesa Kufooketsa anthu kusantula udindo, kusamukira kucipani cina, kucita zinthu zosiyana ndi malamulo, kapena mwinamwake kucititsa kuti pakhale mpando wopamda mwini ndipo pambuyo pake mofulimira kubwerera kundale.

Cacinai, mbali ya Cigawo (4) imafuna sipika kudziwitsa bungwe la Electoral Commission mwakulemba cidizwitso m'kati mwa masiku asanu ndi awiri (7) pambuyo pokhala ndi mpando wa kuimira kolingawiza. Cimeneci citanthauza kucita lipoti sitepe imene imayamba ndi dongosolo loikapo wina.

Cacisanu, mbali ya Cigawo (5) imanena kuti bungwe la Commission liyenera, kudzadza mpando wopanda mwini m'kati mwa masiku makumi asanu ndi anai (90) pogwiritsa nchito munthu wotsatira pa masankho pa cipani candale cimodzimodiz cimene cili pa m'ndandanda wa cipani. M'mawu osavuta kumwa, munthu wotsatira pamezere wa m'ndandanda wacipani akwera kuti

atenge mpando umenewo. Cimeneci ndiyo mfundo yaikulu ya kulowedwa m'malo kwa mipando ya.

Cacisanu ndi cimodzi, mbali ya Cigawo (6) cikucuta zinthu ndi za mndandanda wacipani womwe ulibe anthu aynenera kuimirira pa masankho. Ngati palibe aliyense wotsala pa mndandanda, bungwe la Commission liyenera kupempha cipani kuti citumize mndandanda wina owonjezera m'kati mwa masiku makumi atatu (30). Cigawo cacisanu ndi ciwiri (7) cimanena za malamulo a ziyenerezo ndi mndandanda wa zofunikira zomwe zingagwire nchito to mndandanda wa zofumikira zomwe zingagwire nchito to mndandanda umenewo.

Cacisanu ndi citalu, mbali ya Cigawo (8)bimanena kuti ngati cipani sicitumiza mndandanda wina kukadali nthawi, mpando umenewo sukhala wopanda munthu kwa nthawi yaitali. M'malomwake, bungwe la Commission limapereka mpando uja ku cipani cina candale amene anayenerezedwa pansi pa kacitidwe kogawa mipando. Mbali ya Cigawo (9) cimawonjezera pansi pa mbali ya cigawo (9) cimawonjezzera kuti mavoti a cipani comwe munthu wawo woima ngati prezidenti sadzawerengedwa pogawanso. Colinga cake ceniceni ndi kuletsa cipani kupeza phindu kucokera pa dongosolo ili pomwe akukana kutsatira malamulo a mndandanda.

Cacisanu ndi citatu, mbali ya (10) imanena kuti ngati cipani candale cathetsedwa, kacitidwe ka kuimira kolinganizidwa ka Mamembala a Paliyamenti kokhudzidwa ameneo sakhalanso Membala wa Paliyamenti, ndipo mpando umaperekedwa ku cipani cina comwe uyenerezedwa pansi pa kactitidwe kameneka. Cimeneci citanthauza kuti mpanfo umwenewo udzakhala wa kapangidwe ka cipani, osati kukhala mpando wa MP payekha.

Potsirizira, mbali ya Cigawo (11) imanena kuti ngati mpando wopanda mwini wapezeka m'kati mwa masiku 180 masankho a dziko asanacitike, mpando umenewo sudzalowedwa m'malo. Codziwika apa ndi copewa kusankha wolowa m'malo kwa nyengo yocepa yotsala pomwe Paliyamenti isatsekedwe.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci citanthauza kuti kacitidwe ka kuimira kolinganizidwa ka MP ndi kogwirizana kwambiri ku zipani zawo zandale. Iwo angacoke pa mipando yawo mosavuta kusiyana ndi mmene ma MP a Konsitichuwensi angacitire ndipo cipani cili ndi mphamvu zowaitamanso, kuwalora m'malo, kapena kutaya mpando umenenwo ngati cipani cilepera kutsatira malamulo a mndandanda. Cimeneci cimalimbitsa mwambo wa cipani ndipo cimasunga dongosolo la Kuimira Kolinganizidwa kukupenya pa zocita ndi mindandanda ya cipani kuposa pa munthu payekha. Pa nthawi imodzimodzi, cimacepetsa ma MP kukhala womasuka pa Kuimira Kolinganizidwa cifukwa kukhala kwawo mu Paliyamenti kumadalira kwambiri pa cipani.

Caciwiri, Paliyamenti ndi yotetezedwa kucokera ku mipando yosakhala ndi anthu kwa nthawi yaitali ndi masankho acibwereza a mipando ya Kuimira

Kolinganizidwa, cifukwa mpando wopanda mwini umapatsidwa kwa winawake kucokera ku cipani m'malo mokhala ndi masankho acibwereza. Cimeneco cimagwiritsa nchito dongosolo ili kukhala lofulumira kwambiri ndiponso lotheka kwambiri, ngakhale kuti kuti cimeneci cimatanthauzanso kuti anthu akuimiridwa kupitira mu mndandanda wa cipani kuposa ndi kusankha mwacindunji poikapo mlowam'malo. Lamulo lakuti palibe kudzadza pomwe Paliyamenti ili pafupi kutsekedwa limapereka ganizo lofuna kusunga nthawi ndi zinthu zofunikira pomwe mpando ukhala wopanda mwini mocedwa kwambiri kumapeto a nyengo ya paliyamenti.

Cimeneci citanthauza kuti mipando yoperekedwa ku zipani zandale pansi pa dongosolo la kuimira kolinganizidwa kumakhala kwa cipani candale ndipo osati kwa Membala wa Paliyamenti payekha.

Ngati Membala wa Paliyamenti wasiya ofesi, wafa, watula udindo, kusayenerezedwa, kapena wacotsedwa ndi cipani candale, mpando umenewo sumakhala wopanda munthu kwa nthawi yaitali. Bungwe la Electoral Commission liyenera kuiapo munthuyo ndi wina yemwe ali pa mndandanda kotero kuti cipani candale cipitiriza kusunga mpando womwe cinapambana pa nthawi ya masankho.

Lamulo limalimbikitsanso zipani zandale kuti zizikhala ndi anthu owalowa ali okonzeka. Ngati cipani cilephera kupereka maina pomwe akufunika, cipani cimeneco cingalandidwe mpando umenewo ku cipani cina candale comwe cayenerezedwa.

Kuwonjezera pamenepa, Mamembala a Paliyamenti amene alephera pa mipando yawo cifukwa colakwitsa malamulo kwakukulu sangabwerere ku Paliyamenti kapena kukhala ndi ofesi lalikulu pa nthawi ya utali wa paliyamenti.

Lamulo ili limanenanso  kuti ngati cipani candale cathetsedwa, mipando yawo ya kuimira kolinganizidwa imatengedwa ndi kugawidwa pakati pa zipani zina zoyenerezedwa. Komabe, ngati mpando wopanda mwini wakhalapo pomwe masankho dziko [general elections] ali pafupi, mpando umenewo udzangokhala wopanda munthu kufikira pomwe dziko liponyanso masankho.

### 20. Section 36I – Vacancy for councillors in proportional representation electoral system

**Legal Text**

*(1) Article 157 (1) and (2)(b), (c), (e), (f) and (g) of the Constitution shall apply in relation to a vacancy of a councillor under the proportional representation electoral system.*

*(2) In addition to the grounds specified under subsection (1), a political party that sponsored a councillor holding a seat under the proportional representation electoral system may recall the councillor at any time during the term of a council.*

*(3) Where a vacancy occurs in the office of a councillor, the —*

*(a) Town Clerk or Council Secretary of the local authority shall, within seven days of the occurrence of the vacancy, inform the Commission, in writing, of the vacancy; and*

*(b) Commission shall, within ninety days of the vacancy, fill a vacancy with the next available candidate on a party list of a political party that holds the seat.*

*(4) The Commission shall, where a party list of a political party has no remaining candidates during the term of a council, request the political party to submit an additional party list within thirty days of the request.*

*(5) Sections 36C and 36F shall apply to an additional party list referred to under subsection (4).*

*(6) The Commission shall, where a political party fails to submit an additional party list within the period specified under subsection (4), re-allocate the vacant seat to a political party that qualified for a seat in accordance with the formula for distribution under section 36B.*

*7) The votes obtained by a presidential candidate of a political party that fails to submit an additional party list under subsection (6) shall not be considered in the distribution of seats.*

*(8) A councillor holding a seat for a political party under the proportional representation electoral system shall, where a political party is dissolved, cease to be a councillor and the seat shall be re-allocated to a political party that qualifies for a seat in line with the formula for distribution of seats under section 36B.*

*(9) A vacancy occurring in accordance with this section within one hundred and eighty days preceding a general election shall not be filled.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo ili likulongosola cimene cimacitika pamene khansala amene wasankhidwa kupyolera mu dongosolo la kuimira kolinganizidwa wacoka mu ofesi kapena walephera kupambana pa cisankho.

Khansala yemwe wasankhidwa kupitira mu cipani candale angataye [angalunze] mpando wake cifukwa ca zifukwa zomwe zaperekedwa kale mu Konsitityushoni, ngati kutula udindo, kusayenerezedwa, kapena mfundo zina za lamulo. Kuwonjezera pamenepo, cipani candale comwe cinalipirira khansala, cili ndi mphamvu kuitananso kapena kucotsa khansala ameneyo nthawi iliyonse m'kati mwa nthawi utali wa khonsolo.

Pamene mpando wa khansala wopanda mwini [wopanda munthu], a Town Clerk kapena a Council Secretary ayenera kudziwitsa ungwe la Electoral Commission mwakulemba m'kati mwa masiku asanu ndi awiri [7]. Pambuyo polandira uthenga umenewu, bungwe la Electoral Commission liyenera kuikapo munthu

wina m'kati mwa masiku 90 mwakusankha wina amene alipo kucokera pa mndandanda wa cipani candale. Cimeneci cimatsimikiza kuti cipani candale cisunga mpando womwe cinapeza poyamba.

Ngati cipani candale cili ndi maina owonjezera otsala pa mndandanda wawo, bungwe la Electoral Commission lidzapempha cipani cimenco kuti citumize mndandanda wina m'kati mwa masiku makumi atatu [30]. Mndandanda watsopanowu uyenera kutsatira malamulo amodzimodzi omwe anagwiritsidwa nchito pa mndandanda woyamba.

Komabe, ngati kuti cipani candale calephera kutumiza mndandanda wina m'kati mwa nyengo yofunikira, mpando wopanda mwini udzaperekedwa ku cipani cina candale comwe ciyeneretsedwa panso pa dongosolo logwiritsidwa nchito pogawa mipando ya kuimira kolinganizidwa. Pa cocitika cimeneci, mavoti olandiridwa ndi anthu oima pa uprezidenti wa cipani candale comwe cinalephera kutumiza mndandanda sadzaganiziridwa pogawiranso mipando.

Lamulo ili limanenanso kuti ngati cipani candale cathetsedwa, khansala aliyense yemwe ali pansi pa mpando wa kuimira kolinganizidwa amalandidwa mpando umenewo, ndipo mpandowo umagawidwira ku cipani candale coyenerezedwa.

Ngati mpando wopanda mwini ukucitika m'kati mwa masiku 180 masankho a dziko asanacitike, mpando umenewo sudzadzadzidwa cifukwa dziko likonzekera masankho atsopano.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Lamulo latsopano ili likutanthauza kuti pamene khansala wasankhidwa kupitira pa kuima kolinganizidwa, wasiya ofesi kapena walephera mpando wake, bungwe la Electoral Commission liyenera kudziwitsidwa m'kati mwa masiku asanu ndi awiri, ndipo mpando umenewo uyenera kudzadzidwa m'kati mwa masiku makumi asanu ndi anai [90] pogwiritsa nchito mndandanda wacipani candale kotero kuti mpando umenewo upitiriza kukhala wacipani cimeneco.

Cimeneci cithandiza kusunga makhonsolo kugwira nchito popanda kucedwa, kutsimikiza kuti zipani zandale kukhala ndi udindo wosunga mndandanda wawo wa anthu oima pa masankho kukhala wolembedwa bwino, ndi kumatsimikiza kuti mipando imakhala ndi cipani comwe cinapambana pa mavoti, kucinjiriza kutayika kosayenere kapena kusagwiritsa nchito mipando imeneyo.

**PART VI – RETURNING OFFICERS AND PRESIDING OFFICERS**

**22. Repeal and Replacement of Section 37/Appointment of returning officer- Kucotsa Ndi Kuikapo Lamulo Lolowa M'malo 37**

**Legal Text**

*The principal Act is amended by the repeal of section 37 and the substitution therefor of the following:*

*37. The Commission shall appoint a returning officer, in respect of each constituency, district or ward, by notice in the Gazette.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo lakale linali kunena kuti pambuyo polengeza tsiku lamasankho, bungwe la Electoral Commission lingasankhe munthu woyang'anira [*presiding officer*] masankho pa malo ovotera [*polling station*] (malo oponyera masankho).

Lamulo latsopano limeneli likucotsa lamulo lakale ndipo m'malo mwake likufuna kuti bungwe la Electoral Commission kusankha munthu wobweza masankho kapena *returning officer* pa konsitichuwensi, cigawo, kapena wadi kupyolera mu zidziwitso zofalitsidwa mu Government Gazette. Nchito yawo iphatikizapo kuyang'anira zocitika za masankho, cisamaliro ca kulembetsa, kuyang'anira akuluakulu a mvoti, kutenga ndi kulinganiza bwino zotsatira, ndi kusamalira zoyang'anira masankho m'deralo.

Mawu osavuta, lamulo likusintha kucokera popenyetsetsa pa cisamaliro ca malo oponyera masankho pa konsitichuwensi, pa cigawo, ndi pa mlingo wa wadi. Lamulo latsopano likulolanso bungwe la Electoral Commission kuti liike anchito amenewa popanda kulindira tsiku la masankho kulengezedwa, limene lingacititse kukonzekera ndi kulumikizana pa masankho.

Cinthu cina cofunikira kusintha ndi kalembedwe ka nchito komwe kayenera kufalitsidwa mu Gazette. Cimeneci cimacititsa dongosolo kukhala lipamwamba ndiponso loyera cifukwa anthu onse ndi zipani zandale zingadziwe kuti ndani walembedwa nchito kuti asamalire dera la masankho.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cikonzero cimeneci ciwonjezera kupatsa bungwe la Electoral Commission nthawi yaikulu ya masankho mwakulola nchito kucitika masiku a masankho asanalengezedwe. Komabe, cifukwa ca yobweza masankho, [ returning officer] idzakhala ndi ulamuliro waukulu pa masankho m'madera awo, ndipo pangakhalenso madandaulo a kusakondera kapena kusagwiritsa nchito bwino mphamvu ngati kusasamala sikupitirzidwa.

**23. Insertion of Sections 37A and 37B**

**Legal Text**

**Powers and duties of returning officer**

*37A. (1) A returning officer shall be in charge of electoral activities at a constituency, district or ward.*

*(2) Despite the generality of subsection (1) a returning officer shall —*

*(a) conduct the nomination process at constituency, district or ward level;*

*(b) collate results in a constituency, district or ward;*

*(c) declare National Assembly and local government election results;*

*(d) announce presidential results in a constituency; and*

*(e) perform any other election related duties as determined by the Commission and under this Act.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Munthu wobweza masankho kapena returning officer, ali ndi udindo wosamalira masankho mu konsitichuwensi, m'dera, kapena mu wadi. Nchito yawo imaphatikizapo kuyang'anira ndi kusamalira zocitika zonse za masankho m'dera lawo, kusunga mapepala olembetsera anthu odzaimirira pa masankho, omwe avomerezedwa kudzapikisana pa masankho, ndi kutenga pamodzinso kusonkhanitsa zotsatira za masankho kucokera m'malo onse oponyera mavoti. Iwo alinso ndi udindo wolengeza wopambana ku National Assembly ndi ku boma laling'ono *[local government]* pa masankho m'dera lawo, ndi kulengeza zotsatira za masankho a prezidenti ku konsitichuwensi. Kuwonjezera pamenepo, iwo amacita nchito zina za masankho zoperekedwa ndi bungwe la Electoral Commission. Mwacidule, munthu wobweza masankho amatsimikiza kuti zotsatira za masankho m'dera lawo zacitidwa bwino ndipo kuti dongosolo la zotsatira zake lalengezedwa.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci citanthauza kuti lamulo limanena za nchito ya returning officer, amene ali ndi udindo wosamlira masankho pa mlingo wa konsitichuwensi, pa mlingo wa dera ndi pa mlingo wa wadi. Cimeneci citanthauza kuti dongosolo la kulembetsa anthu, kuwerengera masankho, ndi kulengeza zotsatira za masankho akuyang'aniridwa ndi kugwirizanitsidwa ndi munthu waudindo m'dera lililonse.

Lamulo laling'ono ili likuthandiza kutsimikiza kuti masankho akucitidwa m'njira yolondola, yotheka ndi m'kacitidwe koyenera, ndiponso mwakucepetsa msokonezo, ndi kuwopsa kwa kusasunga bwino zotsatira za masankho. Cimatsimikizanso kuti zotsatira za masankho zitengedwa moyenera, kutsimikizidwa, ndipo ndi kulengezedwa m'njira yoona mtima ndi yocilungamo.

Kuwonjezera pamenepa, lamulo ili likulimbikitsa kuwerengera, kuona mtima, ndicidaliro ca anthu onse pa dongosolo la masankho cifukwa pali munthu waudindo woyang'anira ndi kuwerengera pa zocitika za masankho m'dera lililonse. Kwenikweni, lamulo ili likukweza kacitidwe kosamalidwa ka masankho omasuka, osakondera, okhulupirika mwakupereka nchito ndi maudindo kwa a *returning officer.*

**24. Appointment of Presiding Officer**

*37B. The Commission shall, after prescribing a date for an election, appoint a presiding officer for each polling station at which the election is conducted.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Pambuyo pakuti bungwe la Electoral Commission lakonza tsiku la masankho, liyenera kusankha munthu woyang'anira masankho kapena *presiding officer*, pa malo aliwonse oponyera mavoti. Munthu ameneyu, ndi munthu yemwe ali ndi udindo woyang'anira ndi kusamalira zocitika za cisankho patsiku lamasankho.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci citanthauza kuti malo aliwonse ocitira mavoti adzakhala ndi munthu wotsimikizika waudindo woyang'anira dongosolo la kuponya mavoti, motero kutsimikiza kuti masankho akucitidwa moyenera ndi kuyang'aniridwa kuyambira m'malo momwe anthu amakhala.

Pali kuwerengera kwabwino pa malo aliwonse ovotera cifukwa munthu woyang'anira, *presiding overseer*, ali ndi udindo wa kavotedwe, kusunga cilungamo, kuthandiza anthu ovota monga momwe kungafunikire, ndi kutsimikiza kuti mavoti akuponyedwa m'bokosi ndipo akuwerengeredwa kulingana ndi lamulo. Cimeneci cimathandiza kucepetsa msokonezo, zinthu zosafunika, ndi kutaya ulemu pa nthawi ya masankho.

Lamulo ili likukweza kuona mtima, kutheka kwa nchito, ndi cidaliro ca anthu onse pa dongosolo la masankho cifukwa anthu ovota amatsimikiza kuti munthu woikidwa pa nchitoyo ndi wotsimikiza kuti masankho adzacitidwa mosakondera ndi moyenera pa malo ovotera aliwonse.

**PART VII – VOTING, COUNTING, AND RESULTS**

**25. Amendment of Section 60**

**Legal Text**

*Section 60 of the principal Act is amended by the deletion of subsection (6) and the substitution therefor of the following:*

*(6) A voter shall, once the voter has received a ballot paper referred to under subsection (5)*

*(a) enter an empty voting booth;*

*(b) mark the ballot paper in a way that indicates the candidate the voter intends to vote for;*

*(c) fold the ballot paper to conceal the voter's vote;*

*(d) cast the ballot paper in the ballot box; and*

*(e) without delay, leave the voting station*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Malamulo akale ndi atsopano onse akulongosola cimene munthu wovota ayenera kucita pambuyo palandira mapepala a mavoti pa malo ovotera. Kacitidwe kameneka m'malamulo onse ali pafupifupi ofanana, koma lamulo latsopano likucititsa mawu aang'ono ndi kapangidwe kake asintha kuti akhale atsopano ndi osavuta kulondola.

Pansi pa lamulo lakale, pambuyo polandira mapepala a mavoti ocongedwa ndi munthu woyang'anira, munthu wovota amalowa m'malo ngati kacipinda, mwacinsinsi *aconga pa munthu yemwe afuna kuvotera*, apeteka pepala lovotera kuti libise voti lake, kuliika mu baloti bokosi, ndipo ndi kucokapo nthhawi yomweyo pa malo ovotera.

Lamulo latsopano likusunga dongosolo limodzimodzi, koma lisintha mawu ena ndi kaembedwe ka ciganizo. M'malo monena kuti "voting zompartment", ilo tsopano ligwiritsa mawu akuti "voting booth." Mawu onse awiri atanthauza mawu acinsinsi komwe munthu angaponye voti mwacinsinsi.Lamulo latsopano likucotsanso mawu a kapandawini "yocongedwa pansi pa cigawo (5) (c )" ndiopo m'malo mwakungoti "pepala la ballot limene illi pansi pa cigawo (5)."Cimeneci cikulitsa ndi kumveteketsa bwino mawu kotero kuti angagwire nchito, ku baloti pepala lomwe limaperekedwa kwa munthu wovota.

Kusintha kwina ndi mawu onena za kusankha munthu wovotera. Lamulo lakale limanena kuti munthi wovotera ayenera kusonyeza munthu amene iye "afuna kumuvotera,' pomwe lamulo latsopano limena kuti, "alingalira kumuvotera." Ngakhale kuti tanthauzo la mawu amenewo ndi lofanana, mawu atsopano ndi wolunjika ndipo ndi atsopano.

Kusintha kothera kwenikweni ndi nkhani ya umisiri. Mu lamulo lakale, ndime yothera inalembedwa "(f)" ngakhale kuti panalibe ndime "(e)', imene inali cabe kulakwitsa polemba. Lamulo latsopano lakonza pamenepa ndi kulemba ndime yothera kukhala ngati "(e)".

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Kukonza kumeneku kukucititsa kalongosoledwa kukhala lolongosoka ndi losavuta kumvetsetsa mwakugwiritsa nchito cilankhulo copepuka pokenza zolakwika. Cimeneci cimacititisa kukhala kosavuta kumvetsa zinthu zokhudza lamulo ndi kuceptsa msokonezo kapena mikangano pa kalongosoledwe kovotera. Lamulo ili limalimbitsanso mfundo zofunikira za demokirase ngati cindindi ca voti, kuvota mwadongolo, ndi cisamaliro ca malo ovotera mwakufuna anthu ovota kucokapo pa malo ovotera pambuyo poponya voti. Zonsezi

zikucititsa kuti kusintha kumeneku kukonze mawu ndi kalembedwe ka lamulo popanda dongosolo lenileni lovota kapena ufulu wa anthu ovota.

### 26. Amendment of Section 68/ Lamulo Lokonzedwa 68

**Legal Text**

*Section 68 of the principal Act is amended by the deletion of—*

*(a) the marginal note and the substitution therefore of the following:*

*Counting of votes and announcement of results; and*

*(b) subsection (3) and the substitution therefor of the following:*

*(3) A presiding officer shall mark "rejected" for a rejection on the back of each rejected ballot paper and file the rejected ballot paper separately.*

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo ili likusintha Cigawo 68 mwakulembanso manotsi a pambali pa cigawo ndi kulongosola mmene mabaloti epa ayenera kusungidwira pa nthawi yovota.

Lamulo ili likunenanso kuti pamene mabaloti pepa akanidwa pa nthawi yowerengera mavoti, presiding officer ayenera kulemba liwu "okanidwa" kumbuyo kwa abaloti pepa ndi kulisunga pambali pa mabaloti pepa abwino. Cimeneci cimathandiza mosavuta kuzindikira mavoti okanidwa ndi kutsimikiza kuti kacitidwe kowerengera ndi kolondola, koona mtima ndipo kosavuta kutsimikiza.

Cikonzero ca mutu wa kusintha (zolemba za pambali) za cigawo cocokera pa "Kuwerengera mavoti ndi kulengeza za zotsatira zoyambirira" kukafika ku "Kuwerengera mavoti ndi cilengezo ca zotsatira," cikucotsapo liwu "zoyambirira," lomwe likucititsa kumveka kuti cigawo cimeneco cikucita ndi kuwerengera ndi kutsimikiza zotsatira za masankho. Kusintha kumeneku kukulowa m'malo kukanidwa kofunikira kuconga kotero kuti m'malo moconga, "A kukanidwa," munthu woyang'anira ayenera kungoconga kuti "okanidwa" kumbuyo kwake kwa baloti pepa ndipo liikidwe mu faelo palokha.

Lamulo lakale la pansi pa Cigawo 68 limafuna kuti munthu woyang'anira [presiding officer], pambuyo poponya mavoti, kutsegula mabokosi a mabaloti pepa, kusonkhanitsa mapepalawo kulinga ndi masankho aliwonse ocitidwa pa malo ovotera, kulinganiza mabaloti pepa ndi aja omwe anaperekedwa, kuwerengera mavoti a cisankho ciliconse, ndipo ndi kulengeza ndi kufalitsa zotsatirazo m'manambala ndi m'mawu pa malo oponyera voti.

Limanenanso kuti mabaloti pepa angakanidwe ngati munthu yemwe iwo anadziwa ngati wovota, anali ndi mavoti oculuka kuposa munthu winayo, mavoti osacongedwa, anacongedwa m'njira yomwe inapangitsa kuti munthu wakuti anthu amuvotere likhale losadziwika bwino,silinakhale ndi cizindikiro

codziwika, kapena kuti mabaloti pepa amenewo sanali mabaloti pepa oyenerezedwa ndipo ngati anacongedwa ndi lembo “A okanidwa” kusiyana ndi kulemba kumbuyo kwake “okanidwa.”

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci citanthauza kuti dongosolo lowerengera mavoti pa malo oponyera mavoti limakhala pa nthawi imodzimodzi, pmwe mabaloti pepa asonkhanitsidwa, kuwerengedwa, ndipo zotsatira zake kulengezedwa ndipo mavoti osalongosoka akukanidwa ngati sakuoneka bwino, ndi osacongedwa kapena akusonyeza pamalo posankha pawiri.

Kuwonjezera pamenepo, lamulo ili lasinthidwa m’njira ziwiri, liwu “loyembekezera” lacotsedwa pa mutu [zolemba za pambali], lomwe licititsa kuti zotsatira kumveka pothera pomwe zilengezedwa pa malo oponyera voti. Cizindikiro cokanira casinthidwa kucokera pa “A wa kukanidwa” ndi kukhala cabe “kukanidwa,” ndi kupangitsa ilo kukhala lopepuka ndi losavuta kugwiritsa nchito. Lamulo ili likuthandiza kupanga dongosolo ili kukhal losavuta, lopepuka ndi lodziwika, ndi kucepetsa msokonezo wojambula zotsatira ndi mabaloti okanidwa.

**27. Amendment of Section 70 - Lamulo Lokonzedwa 70**

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**
Lamulo latsopano ili lasintha mwakucotsa ndi kulowedwa m’malo ndi zolemba za pambali za manotsi Cigawo 70 cocokera pa “zotsutsa zokhudzana ndi kuwerengera kwa mavoti ndi cilengezo ca zotsatira zoyembekezera,” kukafika pa “Zotsutsa zokhudzana ndi kuwerengera kwa mavoti ndi cilengezo ca zotsatira za masankho.”

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci citanthauza kuti lamulo ili likulongosola za ganizo lake. Kumbuyoku, mawu a mtsinde onenedwa, anali kutanthauza kuti zotsutsa zingangokhudzana ndi dongosolo la kawerengeredwe ndi kulengeza zotsatira zoyembekezera. Mbali imene inakonzedwa ya zolemba za pambali, tsopano ikucotsapo kuiika malire komwe kunalipo kocitidwa ndi liwu “zoyembekezera” ndipo limacititsa kuti zimenezi zikhale zotsatira zoyenera. Cimeneci cikusonyeza colinga cocitidwa ndi lamulo pofuna kutsimikiza kuti zitsutso zipitirize kupyola zotsatira ndipo zingagwire nchito pa cilengezo cothera ca zotsatira za masankho.

**28. Amendment of Section 71-Lamulo Lokonzedwa 71**

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo ili lasinthidwa mwakucotsa zolembedwa za pambali zomwe zimanena kuti "Kalongosoledwe kokhudza zotsatira zoyembekezera ndi zinthu zovotera," ndipo lalowedwa m'malo ndi "Kalongosoledwe kokhudzana zotsatira za masankho ndi zinthu za mavoti."

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci citanthauza kuchula dzina lakuti zolembedwa za pambali zicititsa kukhala kosavuta kumvetsetsa mwakucotsa liwu "zoyembekezera." Lamulo lakumbuyo la zolemba za pambali linali kungocititsa zotsatira zosakhalitsa pa malo oponyera mavoti. Kukonzanso kukuwonjezera ganizo kotero kuti kalongosoledw ka lamulo, tsopano kangagwire nchito pa zotsatira zonse za masankho, popanda kusiyanitsa pakati pa zoyembekezera ndi manambala a zotsatira zothera. Kuwonjezera pamenepo, malamulo ang'ono osungira ndi kuyendetsa zinthu zovotera tsopano zimakhudza dongosolo mosiyana ndi mbali yoyambirira.

**29. Amendment of section 72 / Lamulo Lokonzedwa 72**

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo ili likusintha mwakucotsa Cigawo 72(1) ndipo likunena kuti nchito za *returning officer* pambuyo polandira zinthu za masankho pansi pa Cigawo 71. M'mawu osavuta, pambuyo poti returning officer watenga zotsatira za masankho kucokera *m'mapolling station*, ayenera kuwerengera ndi kulinganiza zotsatirazo pa konstichuwensi, pa cigawo kapena pa wadi, ndipo pambuyo pake kupenyetsetsa momwe zimenezo zilili m'njira yomwe lamulo limafunira. Colinga cacikulu ca dongosolo losungira zotsatira za masankho kukhala zomveka bwino ndipo ndi kucititsa mawu a lamulo mogwirizana ndi masankho motsatira lamulo.

Polinganiza ndi Cigawo 72(1) cocotsedwa mu lamulo lakale, lamulo latsopano ndi lalikulu ndipo lili ndi mfundo zambiri. Lamulo lakale limachula cabe za kulengezedwa kwa zotsatira za masankho a prezidenti ndi meya kapena wakumpando wa khonsolo, ndipo linali kungotsimikiza zotsatira za National Assembly ndi masankho a Wadi. Lamulo latsopano limaphatikizapo masankho a prezidenti, Memb.ala wa Paliyamenti, Meya, Wakumpando wa Khonsolo ndi Khansala pa nthawi yolengezera. Ndiponso, limatsimikiza kunena za zotsatira za Membala wa Paliyamenti, Meya, Wakumpando wa Khonsolo kapena masankho a Khonsolo omwe ayenera kutsimikizidwa.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Lamulo losinthidwa likukonza kamvekedwe ndi kutsimikiza kwa lamulo m'dongosolo lamasankho. Anthu obweza masankho a returning officer tsopano ndi otsimikiza za malangizo a pomwe zotsatira ayenera kulengezedwa ndipo ayenera kutsimikizidwa, cimene cingacepetse msokonezo ndi kusagwirizana pa konsitichuwensi, pa cigawo ndi pa mlingo wa wadi. Cimathandizanso kutsimikiza kuti mbali zonse zogwirizana zotsatira za masankho dera ndi a dziko zikusungidwa pansi pa kalongosoledwe kamodzi komwe kangacepetse mikangano ndi kucititsa kuti dongosolo la kuwerengera ndi kutsimikiza likhale loona kwambiri.

**PART VIII – VOTER EDUCATION AND NOMINATION PETITIONS**

**30. Repeal and replacement of section 80 - Kucotsa Ndi Kuikapo Lamulo Lolowa M'malo 80**

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo latsopano likukulitsa udindo wa bungwe la Electoral Commission mwakufuna kupereka maphunziro a masankho, kusiyana ndi kucita tero pa nyengo ya masankho yokha. Kusiyana ndi lamulo lakale, lomwe linali ndi maphunziro ocepa a otsimikiza masankho, lamulo latsopano likulola bungwe la Commission kuphunzitsa anthu mosolekeza pa nkhani za kalongosoledwe ka kavotedwe, ufulu wa wovota, kalembetsedwe, ndi kutengamo mbali kwa demokirase. Lamulo lokonzedwanso ili likusintha maphunziro a anthu ovota kucokera pa zocitika za kanthawi ndi kukhala nchito yopitiriza ya bungwe la Commission.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Lamulo latsopano likukonza kamvedwe ka anthu onse ka dongosolo la masankho mwakulola maphunziro a mavoti mosalekeza. Cimeneci cingawonjezere kudziwa, kutengamo mbali ndi kumvetsetsa kalongosoledwe ka mavoti, pa nthawi imodzimodzi kucepetsa kupereka uthenga wolakwika ndi msokonezo pa nthawi ya masankho. Kuwonjezera pamenepa, bungwe la Electoral Commission lidzakhala ndi udindo waukulu ndipo lingafune zinthu zambiri zofunikira, kukonzekera ndi kufikira anthu ambiri mu mapulogiramu opitiriza a masankho. Komabe, kupitiriza kwa kacitidwe kameneka kangalimbikitse demokirase mwakupanga anthu odziwa ndi ovota ocita bwino.

**31. Insertion of Part VIIIA- NOMINATION PETITIONS**

**Zoikidwamo za Mbali 8 ~ KULEMBETSA MADANDAULO.**

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Mbali yatsopano ya VIA, yawonjezedwa kuti idziwitse za pempho la kulembetsa, lomwe ndi dandaulo loperekedwa ku bwalo lamilandu kapena ku bungwe laulamuliro, kutsutsa za kulembetsa kwa munthu wina pa masankho. Cimeneci cimacitika kawirikawiri ndi munthu yemwe amakhulupirira kuti anavomerezedwa molakwika kapena kulembetsa mophwanya lamulo la masankho.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci citanthauza kuti lamulo lakale lasintha mwakuwonjezera Mbali yatsopano VIA, pambuyo pa Mbali VIII. Mbali iyi yatsopano ili ndi zina zowonjezera zokhudzana ndi Nomination Petition imene tsopano imalola anthu kutsutsa kalembetsa kwa munthu wokaima pa masankho, pomwe masankhowo asanacitike, ngati akhulupirira munthuyo anavomerezedwa kapena sakwanitsa zofunikira za lamulo.

Cimenecicimacititsa kuti masankho akhale osakondera mwakutsimikiza kuti ndi anthu okha oyenerezedwa omwe angaloledwe kuima pa masankho. Cimakwezanso kuona mtima ndi kuwerengera pa dongosolo la kulembetsa cifukwa bungwe la Electoral Commission pamodzi anthu odzima pa masankho angafunsidwe ndi kubwerezedwa ndi bwalo lamilandu ngati zolakwa kapena zocitika zosalondola lamulo zilipo.

Lamulo ili likuwonjezera kuthandiza kucinjiriza mikangano pambuyo pa masankho, cifukwa mavuto okhudzana ndi kuyenerezedwa kwa munthu kungathetsedwe mwamsanga, masankho asanacitike. Pa zonsezi, limalimbikitsa cidaliro pa dongosolo la masankho, kutsimikiza kuti malamulo polembetsa akutsatiridwa bwino.

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Ngati munthu wina akufuna kutsutsa za kulembetsa kwa munthu wodzaima pa masankho mu bwalo lamilandu kapena ku khoti latribunal, ayenera kutumiza pempho la nomination petition pogwiritsa nchito mapepala a boma ndi kalongosoledwe kofunika ndi lamulo.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci citanthauza kuti lamulo latsopano lomwe lawonjezedwa likuthandiza kucititsa kuti kasungidwe ka mikangano ya masankho ikhale olinganizidwa, osakondera, ndipo osasintha cifukwa madandaulo sangapangidwe popanda umboni. Anthu ayenera kugwiritsa nchito njira zoyenera ndi kalongosoledwe koikidwa ndi lamulo. Cimeneci cimathandizanso mabwalo a milandu ndi matribunal kuthana ndi mikangano yakulembetsa bwino masankho ndi

moyenera, pomwe akuteteza msokonezo, zodandaula zabodza, kapena kusagwiritsa bwino dongosolo la lamulo.

## 32. Rules relating to nomination petition - Malamulo Okhudzana ndi Kulembetsa Madandaulo

### Mawu Alamulo Osavuta Kumva

Lamulo ili likupatsa mphamvu amfumu a Chief Justice kuti apange malamulo momwe dandaulo la nomination petition.

### Kodi Cimeneci Citanthauzanji?

Lamulo limeneli limapatsa mphamvu a Mfumu a Bwalo Lamilandu a Chief Justice kuti apange malamulo, kupyolera pa kukhazikitsidwa kwa lamulo, kutsogolera kacitidwe ndi kalongosoledwe kolembetsera ndi kumvera za madandaulo pamaso pa bwalo lamilandu kapena *tribunal*. Malamulo aang'ono angatenge nthawi yaitali kuti alondoledwe, ndalama za ndapusa, ndalama zolipira bwalo lamilandu, pamodzi ndi nkhani zina zilizonse zofunikira ngati kungafunike kuti pakhale cisamaliro cotheka ca madandaulo, ndipo cimacititsa kapangidwe ka lamulo kocitira ndi mikangano ya kalembetsedwe ka lamulo. Lamulo limeneli limapereka citsimikizo cakuti munthu aliyense yemwe wapereka dandaulo, ali ndi ufulu wokaonekera mu bwalo lamilandu kapena kapena kuimiridwa ndi munthu wina mu tribunal; ndipo cimeneci cimakweza kusasintha, kutheka, kusakondera, ndi mpata wacilungamo pothetsa mkangano wa masankho.

## 33. Amendment of section 110 - Lamulo Lokonzedwa 110

### Mawu Alamulo Osavuta Kumva

Cigawo 110 cakonzedwa kuti cipange zinthu kukhala zomveka ndi kusintha zomwe bungwe la Commission lingasinthe. Tsopano ilo likunena bwino kuti Lamulo la Khalidwe [kapena Code of Conduct] ndi Lamulo Loyamba Lamndandanda. Likusinthanso cilango coperekedwa cophwanya Lamulo kucokera pa kusayenerezedwa kukafika poimitsa, kutanthauza cipani kapena munthu woima pa masankho angaimitsidwe kwa kanthawi m'malo momucotseratu, pomwe akutsimikiza kuti akulondola malamulo.

Cikonzero cimeneci cikusintha mbali ziwiri ku Cigawo 110 ca mfundo ya Lamulo. Coyamba, ilo likumveketsa bwino kuti umboni wa cigawo cacing'ono (1) lili ku Mndandanda Woyamba, osangoti Mndandanda cabe. Cimeneci cikukonza kapangidwe ndi cikupewa msokonezo pomwe Lamulo limenelo lingakhale ndi zambiri kuposa cabe mndandanda. Caciwiri, mu Cigawo cacing'ono (2), liwu

"kusayenereza" lalowedwa m'malo ndi "kuimitsidwa", limene likusintha zotsatira za lamulo ili. M'malo mocotseratu kapena kucinjiriziratu munthu kuima pa masankho kapena kusangalala ndi ufulu, mawu atsopano akupereka ganizo loimitsidwa mwakanthawi ndipo pambuyo pake kuikidwanso.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cikonzero cimeneci cikusintha mbali ziwiri ku Cigawo 110 ca mfundo ya Lamulo. Coyamba, ilo likumveketsa bwino kuti umboni wa cigawo cacing'ono (1) lili ku Mndandanda Woyamba, osangoti Mndandanda cabe. Cimeneci cikukonza kapangidwe ndi cikupewa msokonezo pomwe Lamulo limenelo lingakhale ndi zambiri kuposa cabe mndandanda. Caciwiri, mu Cigawo cacing'ono (2), liwu "kusayenereza" lalowedwa m'malo ndi "kuimitsidwa", limene likusintha zotsatira za lamulo ili. M'malo mocotseratu kapena kucinjiriziratu munthu kuima pa masankho kapena kusangalala ndi ufulu, mawu atsopano akupereka ganizo loimitsidwa mwakanthawi ndipo pambuyo pake kuikidwanso.

**34. Amendment of section 125 - Lamulo Lokonzedwa 125**

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo latsopano likufewetsa Cigawo 125(2)(w) mwakucepetsa mphamvu za bungwe la Commission poika malire. Pansi pa lamulo lakale, bungwe la Commission lingapange malamulo a madera oikidwa malire, makonsitichuwensi, mawadi ndi malo oponyera voti. Mawu a lamulo latsopano akucotsa madera kucokera pa mndandanda umenewo, conco mphamvu za bungwe la Commission zimangogwira nchito m'makonsitichuwensi, mawadi ndi m'malo moponyera voti momwe munaikidwa malire.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci citanthauza kuti lamulo latsopano likumveketsa bwino ndi kuika malire pa ulamuliro wa bungwe la Commission kotero kuti malo omwe anaikidwa malire (kuika mamapu m'malo ovotera kapena kuika malire a makonsitichuwensi) kuti ndi nchito yofunika kupenyetsetsa cabe pa malire a anthu ovota mwacindunji ndi oimiridwa, kusiyana ndi madera onse pamodzi. Madera sakuonedwanso ngati malo omwe bungwe la Commission lingaike malire mwalamulo pansi pa ndime, limene likucepetsa kustsimikizika ndi kucinjiriza bungwe la Commission kusamvetsedwa kukhala ndi ulamuliro pa malire a ovota a madera oikidwa malire. M'mawu ena, lamulo lalimbikira pa madera a makositichuwensi, mawadi ndi malo oponyera voti kusiyana ndi dera lalikulu loyang'anira mu zigawo za madera lomwe linali pansi pa lamulo lakale.

**35. General Amendment - Cikonzero ca Cizolowez**

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Lamulo ili lasintha mawu ena ogwiritsidwa nchito mu malamulo onse. Kulikonse komwe lamulo limagwiritsa nchito mawu "kompatimenti" kapena "kompatimentsi," mawu amenewo tsopano alowedwa m'malo ndi "buufi" kapena "buutsi."

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Cimeneci cikutanthauza kuti lamulo lacititsa cilankhulo cogwiritsidwa nchito mu lamulo cikhale camakono ndi copepuka. Kulowedwa m'malo kwa liwu "kompatimenti" ndi "buufi" kukupanga mawuwo kukhala ofewa kwa anthu oponya masankho, anthu ocititsa masankho pamodzinso ndi anthu onse kumvetsetsa, cifukwa mawu akuti "voting'i-buufi" ndi odziwika bwino ndipo ndi mawu adongosolo la masankho.

**36. Amendment of the Schedule**

**FIRST SCHEDULE**

**DONGOSOLO LOYAMBA**

**(Section 110)**

**Mawu Alamulo Osavuta Kumva**

Cikonzero cimeneci cangosintha mitu mwakuikamo liwu "Coyamba" patsogolo pa liwu "Mndandanda." Kusintha uku sikusiyanitsa zam'kati mwake mwa Mndandanda [Scahedule], koma kungowongolera kuti lamulo limeneli likuloza ku Mndandanda Woyamba.

**Kodi Cimeneci Citanthauzanji?**

Kukonza kumeneku kukuthandiza lamulo labwino m'kati mwa Lamulo mwakusintha mitu kucokera pa "Mndandanda Woyamba," kotero kuti lamulo likumveka mosavuta kuzindikirdwa ndi kutsimikizidwa ndi Mndandanda womwe ukunenedwapo. Kusintha kumeneku kukukhala kofunika cifukwa mfundo yaikulu ya Lamulo lomwe poyamba inali ndi Mndandanda umodzi, koma lamulo latsopano likudziwitsa Mndandanda Waciwiri, kuupanga kukhal wofunika posiyanitsa pakati pa Mindandanda iwiri pofuna kupewa msokonezo ndi kusamasulira kolakwika.

## 35. Insertion of Second Schedule - Coikidwamo ca Mndandanda Waciwiri.

### Mawu Alamulo Osavuta Kumva

Mndandanda Waciwiri ukulongosoledwa mmene mipando yosungidwira azimayi, anyamata, ndi anthu operewera kucita zinthu zina agawana pakati pa zipani zandale pa dongosolo la kuimira kolinganizidwa. Bungwe la Electoral Commission silipereka mipando imeneyi mwacisawawa.

Kacitidwe kameneka kamayamba mwakuwonkhetsa mavoti onse auprezidenti wa zipani zomwe zinayenerezedwa pansi pa lamulo. Mavoti okanidwa amasiyidwa cifukwa samawerengedwa. Pambuyo pake, mavoti onse amagawidwa ndi nambala ya mipando yosungidwa m'gulu lililonse kuti apeze nambala yamlingo [target], imene ndi nambala mavoti ofunikira pa mpando umodzi. Mwacitsanzo, azimayi ali ndi mipando 20, anyamata ali ndi 15, ndipo anthu operwera kucita zinthu zina, conco gulu lililonse lili ndi mlingo wake.

Mndandanda uwu umacititsa kuti cikhale codziwika kuti cipani coyamba ciyenera kukwaniritsa mlingo wake wagulu cisanaganizidwe kupatsidwa mipando m'gulu limenelo. Ngati sicikwanitsa kufika pamlingo wake, cipanico cimatsitsidwa pa mbali imeneyo. Pa mipando ya khonsolo, kacitidwe kamodzimodzi kamagwiritsidwa nchito ngakhale kuti nambla ya mipando mu khonsolo iliyonse imasiyana. Mndandanda wa Matebulo umangothandiza kuonetsa kacitidwe kake. Iwo amathandiza owerenga wamba kuti aone mmene mavoti amasinthira kukhala mipando ya azimayi, anyamata, ndi anthu operewera kucita zinthu zina. Mwacidule, Mndandanda ndi kacitidwe kogawana mipando, komwe kamasintha cicirikizo kukhala kuimiridwa kosungidwa m'njira yosakondera.

### Kodi Cimeneci Citanthauzanji?

Cimeneci citanthauza kuti mndandanda ukulongosoledwa bwino ndipo njira za masamu zowerengera mipando ya azimayi, ya anyamata, ndi anthu operewera kucita zinthu zina pakati pa zipani zandale. M'mawu osavuta, bungwe la Electoral Commission limatenga mavoti a anthu onse oima ngati prezidenti a zipani zoyenerezedwa ndi kuwagwiritsa nchito pa cipani coyenera. Zipani zomwe zili mavoti oculuka zimatenga mipando yambiri, pomwe zija zili ndi mavoti ocepa zimatenga mipando yocepa kapenanso olandira ciliconse.

Poyamba, mipando imawerengedwa pogwiritsa nchito *target* [kapena nambala yoikidwa ya mavoti ofunika pa mpando umodzi]. Ngati cipani cili ndi mavoti "otsalira" pambuyo potenga mipando yonse, mipando ija yotsalira imalinganizidwa ndi zipani zina, ndipo mipando yotsala imapatsidwa ku zipani

zomwe zili ndi mipando yotsalira yambiri. Ngati pakhala kulingana pakati mpando wothera, umenewo umaganizidwa mwaciswawa.

Ganizo lalikulu ndi kutsimikiza kuti mipando yapadera ya azimayi, anyamata, ndi anthu operewera kucita zinthu zina akugawana mosakondera kulingana ndi kuculuka kwa anthu omwe anaponya masankho pa cipani ciliconse.